# UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

NTHAMBI YOONA ZA NYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO


ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'DZINJA LA 2025-2026 M'BOMA LA NTCHEU

## Nyengo ya dzinja ya 2025/2026 Mwachidule

Katenthedwe ka Nyanja ya mchere ya Pacific sikakhudza kwambiri nyengo ya dzinja ya 2025/2026

Boma la Ntcheu likuyembekezereka kulandira mvula ya **mlingo wokhazikika kapena mlingo ochepera okhazikika** mu nyengo ya mvula ya 2025/2026.


## October 2025




Mu mwezi wa October, boma la ntcheu likuyembekezera kulandira Mvula ya mulingo wosapitilira 30mm.

Mvula yoyambilira izakhala ya mphepo yamkuntho komanso ziphaliwali.


## November 2025




Mu mwezi wa November, madera ambiri m'mbomali akuyembekezera kudzalandira mvula ya mulingo wa pakati pa 20 ndi 50mm.

Imeneyi ndi mvula yamlingo okhazikika kapena kuchepera apo.


## December 2025




Madera ambiri mbomali akuyembekezeka kulandira mvula pa mlingo pakati pa 200 ndi 240mm mu Mwezi wa December.

Mvula yokhazikika ikuyembekezeka kuyamba kugwa sabata lachitatu m'mwezi wa December.


## January 2026




Mwezi wa January ndi umene ukuyembekezeka kulandira mvula yambiri mu nyengoyi. Madera ambiri m'mbomali akuyembekezereka kuzalandira mvula yamulingo wokhazikika kapena kuposera apo yokwana 250mm.
Koma madera monga kwa a SC Champiti akhoza kuzalandira mvula yamulingo wokwana 300mm.

Pali kuthekera kwa ng'amba yosaposera sabata imodzi m'mweziwu.


## February 2026




Madera ambiri akuyembekezereka kuzalandira mvula ya mlingo wokhazikika kapena kuchepera apo yokwana pakati pa 150 ndi 200 mm.


Pali kuthekera kwa ng'amba yochepera sabata limodzi.

## March 2026




Madera ambiri akuyembekezereka kulandira mvulo ya mlingo wapakati pa 110 ndi 150mm m'mweziwu.

## April 2026





Nyengo yadzinja ikuyembekezereka kutha sabata loyamba la mwezi wa April, pomwe madera ambiri azakhala akulandira mvula ya mlingo wosapitilira 60mm.

Boma la Ntcheu likuyembekezereka kulandira mvula ya **mlingo wokhazikika kapena mlingo ochepera okhazikika** mu nyengo ya mvula ya 2025/2026. Mvula yokhazikika ikuyembekezereka kuyamba pakati pa mwenzi wa December,, 2025. Nyengo ya mvula ikuyembekezereka kufika kumapeto sabata loyamba la mwezi wa April 2026. Nyengo ya dzinja ikuyembekezereka kukhala yotalika masiku a pakati pa 120 ndi 130. Pali kuthekera kokhala ndi ng'amba yapafupifupi sabata imodzi m'mwezi wa January komanso February.

The table and figure below show monthly rainfall distribution for the season with a normal band in grey.

| NTCHEU | | | |
|---|---|---|---|
| MONTH | NORMAL RANGE | | FORECAST |
| OCT | 9.8 | 44.6 | 19.3 |
| NOV | 66.6 | 123.2 | 44.6 |
| DEC | 182.7 | 319.5 | 218.1 |
| JAN | 270.9 | 432.1 | 235.3 |
| FEB | 163.6 | 252.1 | 202.5 |
| MAR | 127.6 | 199.3 | 189.6 |
| APR | 10.8 | 59.2 | 37.2 |





**Ulosiwu udzaunikidwanso mu December 2025**



For further information contact: The Director of Climate Change and Meteorological Services, P.O. Box 1808,Blantyre.
Tel +265 1 82 47 12 / Cell: +265 882 26 65 79 Email: metdept@metmalawi.gov.mw ; Website: www.metmalawi.gov.mw



Zapangidwa ndi kusindikizidwa mothandizidwa ndi: